

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

UBATIZO WA OKHULUPIRIRA

“Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiyo cha machimo anu...” —Machitidwe 2:38

Kumayambiriro kwa zaka za mma 1500, malaŵi a chikonzedwe cha mpingo anayamba ndipo anafalikira mwachangu ku dera lonse la ku Ulaya pamene Mulungu anayamba kukonzanso chidziwitso cha choonadi cha Mau a Mulungu. Dziko linali lili pa tulo ta uzimu tofa nato kuchokera mu nthawi za mdima za ulamuliro wa apapa a mpingo wa Chikatolika amene anapotoza choonadi cha Mpingo woyamba. Chikonzedwe cha ma Protestant, chimene chinayamba ku dziko la Germany ndi munthu wotchedwa Martin Luther m'chaka cha 1517, chinakula pamene anthu anayamba kuona chinyengo cha Chikatolika. Ambiri mwa iwo amene anakonzanso mpingo, ngakhale sanaone kuwala konse, komabe amalandirabe zidutswa ndi za choonadi cha ziphunzitso ndi machitidwe ena.

Conrad Grebel ndi Felix Manz anali anyamata amene anaphunzira pansi pa Ulrich Zwingli, wa ku Zurich m'dziko la Switzerland amene anagwira ntchito yokonzanso mpingo. Iwo sanagwirizane naye ndi anasiyana chifukwa cha mchitidwe

wakale lomwe wobatziza makanda umene unali kuchitika mu mpingo wa Katolika, ndipo utsutsana ndi mchitidwe wa mu mpingo wa mu Chipangano Chatsopano. Grebel ndi Manz anali anthu amene mwa ena, iwo analandira kuwala, ndi



kumvetsetsa kuti ubatizo womiza m'madzi unali wa iwo amene anali atalapa machimo awo. Iwo anakana za ubatizo wa ana aang'ono chifukwa chakuti anawo sangathe kulapa kapena kukhulupirira, choncho sayenera kubatizidwa.

Palibe ndime kuchokera M'malembo zimene zimanena kuti ana adzibatizidwa kapenanso zitsanzo za mchitidwewu mu Baibulo. Zimaoneka ngati ubatizo wa ana anayamba kumapeto kwa zaka za ma 300 AD ndipo mchitidwewu unavomerezeka

ndi kukula m'zaka za mma 450 AD. Mchitidwewu unakula popeza panali chiphunzitso chonyenga chakuti ana akhoza kupita ku gehena ndipo ubatizo ungawapulumutse ku machimo awo.

Ubatizo wa madzi supulumutsa moyo wa munthu. Ana amakhala wosachimwa pamaso pa Mulungu chifukwa sanachite choipa chilichonse mwadala ndipo adzapita kumwamba ngati amwalira.

Ubatizo wa ana sunawathandize anthu ambiri. Anawo amakula nkumaganiza kuti apita Kumwamba popeza anabatizika ali ana, koma akakula amakhala m'moyo wauchimo. Anthu ayenera kutsukidwa ndi mwazi wa Yesu ndipo asatsamire pa nsanamira ya ubatizo wa ana.

Iwo amene anatsutsana ndi ubatizo wa ana anadziwika kuti anali ma Anabapists (kutanthauza iye amene amabatizanso kangapo kangapo). Ubatizo woyamba unali ubatizo wa ana umene uli wotsutsana ndi malemba. Ubatizo wachiwiri, kapena “kubatizanso” unali ubatizo wa okhulupirira.

Ma Anabaptists anazunzidwa ndi Akatolika komanso ma Protestant chifukwa chobatiza akulu. Felix Manz anazunzika kwambiri

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Mau a Mulungu: Ubatizo wa Okhulupirira

Tsamba 4

Nkhani yotsagana nayo: Mpingo wa Mulungu: Ubatizo wa Okhulupirira

Tsamba 5

Mafunso ndi Mayankho

Tsamba 7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 8

Zimene

BAIBULO

Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

ndipo anaponyedwa m'ndende kambirimbiri chifukwa cholalikira za ubatizo. Pa March 7, 1526, bungwe lolamulira la ku Zurich ku Switzerland linapereka lamulo lakuti kubatiza kachiwiri ndi mlandu umene chilango chake ndi ndi imfa pomizidwa m'madzi. Manz anaponyedwanso mndende. Atatulutsidwa anapitiriza kubatiza ndi kulalikira. Manz anali wokhulupirika ndi womvera ndipo sanafune kugwedezeka pa choonadi ichi ngakhale amakumana ndi otsutsana naye ochuluka.

Pa December 3, 1526, Manz anagwidwanso naponyedwa mndende ya ku Wellenberg. Pa January 5, 1527, anagamulidwa kuti aphedwe pomizidwa m'madzi. Imfa yomizidwa m'madzi imatchulidwa kuti "ubatizo wachitatu." Manz anatengedwa ku mtsinje wa Limmat, ndipo mofuula analemekeza Mulungu nachitira umboni kwa anthuwo. Mbusa wina anafika pafupi ndi pamene panali Manz namuza kuti asiye zikhulupiriro zakezo. Patali cha poteropo, amai ake ndi abale ake anamulimbikitsa kuti ayimebe njii ndi kulolera kufa chifukwa cha Yesu. Manja a Manz anali omangidwa ndipo anawakumaniza ndi mabondo ake ndipo pakati anayika mtengo kuti asamathe kumatakataka. Kenaka anaponyedwa m'madzi muja ndipo anamira. Iye anali Anabaptist woyamba kufa chifukwa cha chikhulupiriro chake. Mbiri imanena kuti mau ake omaliza anali akuti, "Mulungu, m'manja mwanu ndipereka mzimu wanga."

Choonadi cha ubatizo wa okhulupirira sichinabwere mofewa konse ayi. Mulungu alemekezeke chifukwa chobwezeretsanzo choonadi chokoma kwa anthu ake ndi kwa iwo amene ali okonzeka kutaya miyoyo yawo kuti chisatayike. Sakramento la Ubatizo lipitirire kukhala lopatsidwa ulemu ndi lolemekezedwa pakati pa anthu a Mulungu.

mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoonza za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wovomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wovomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo.

Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA

editor@thegospeltruth.us

Mau a Mkonzi



Pamenepo iwo amene analandira mau ake anabatizidwa; ndipo anaonjezedwa tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatu. —Machitidwe 2:41

Kukadakhala kokondweretsa kuona anthu awa okwana 3,000 akubatizika zaka zambiri zapitazo pa tsiku la Pentekoste. Tangoganizani kutalika kwa mizere ya anthu amene anatembenuka mtima akuyembekezera kuti nawonso apeze nawo mwayi wolowa m'madzi. Taonani kusekerera kwake ndiponso tamvani thungululu, kukondwera komanso kuyimba. Imvani kufuula kwa matamando ndipo onani manja ochuluka amene akwezedwa m'mwamba pofuna kulemekeza Yesu Khristu. Izi zinali zodabwitsa ndi zosamvetsetseka kwa iwo amene anali atakana Khristu ndipo amaona zimene zimachitikazo.

Ndimayamika kwambiri kuti ndinapulumutsidwa ndili mwana ndiponso kuti ndinafa ndi Khristu mu ubatizo. Ndili ndi mwayi wakuti ndinabatizako anthu ena: ku mtsinje wa ku Afrika umene munali ng'ona, mu madzi odzaza ndi nyongolotsi zoopsa, mu madzi odikha amatope, mu madzi mitsinje yamadzi oyera mbee, mu mpita wa madzi ku Pakistan, mu Nyanja ya madzi ozizira kwambiri ku Canada komanso mu zitsime zobatizira zopezeka mkati mwa tchalitchi. Ngakhale palibe kusiyana kugawo la uzimu ponena za malo amene munthu abatizirako, ineyo pandekha ndimakonda kubatizira pa malo a madzi abwino achilengedwe kuti ukhale umboni ku dziko lonse.



Ubatizo wanga mu mtsinje wa Santiam ku Oregon ku America

Ulendo uno, ndinafulumizidwa kugawana nanu zoonadi zina za Baibulo makamaka pa mutu wa ubatizo. Mtima wanga ndi wodzala ndi chimwemwe chifukwa cha mtolo wa choonadi komanso kuunika kumene kulipobe kufikira masiku ano. Ubatizo ndi wofunikira ndipo ndaonapo kuti pakati pa anthu ena a Mulungu, pali kuchepa kwa chidwi komanso kusakondweretsedwa ndi ubatizo. Ubatizo sukuyenera kukhala chinthu chimene munthu achite kuchiganizira pamene wangotembenuka mtima. Ukuyenera kukhala chimodzi mwa zinthu zoyambirira kuchita powonetsa kumvera kwake pamene wapulumutsidwa. Mzimu Woyera ayatsenso kufunikira ndi kukoma kwa phunziroli ndi mchitidzewu pakati pa anthu a Mulungu.

Ndikukumbukira mawu a wolemba nyimbo wotchedwa m'bale Ulysses Phillips amene anati: "Ndivomereza za chiukitso, chimene chachitika mkati mwa mtima wanga, Ndadzutsidwa kuchokera kwa akufa, ndipo tsopano ndikhala ndi Khristu...Ha! Yamikani Ambuye chifukwa cha chigonjetso, anandikweza kuchokera ku imfa kupita ku moyo, ndi chikondi chake chachikulu komanso mphamvu zodabwitsa, tsopano Moyo wosatha ndi wangadi." Nyimbo imeneyi imanena momveka bwino za umboni wa chimene ubatizo umayimira.

Pemphero langa ndilo lakuti aliyense wowerenga athandizidwe ndi kulimbikitsidwa pamene alingalira za kukoma ndi tanthauzo la ubatizo.

Michael W. Smith

October 2014

Zambiri Zili pa

INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.us

kuti mudzilandira

makalata athu kapenanso

kuti muone makalata

akale.



Malo a Chikumbutso

Mu Chipangano Chakale, nthawi zambiri anthu amamumangira Mulungu guwa la nsembe iwowo akapambana pa nkondo kapena Ambuye akawayendera mwapaderadera. Guwalo linali malo okumbukira zimene Mulungu anachita.

Ubatizo ukhale ndi malo apaderadera a chikumbutso mmoyo wa mwana wa Mulungu aliyense. Pamene mdierkezi ayesa, apereka chiyesero ndi kulimbana ndi chikhristu chanu, ndi mdalitso waukulu kwambiri kwa inu pamene muyang'ana kumbuyo ku nthawi imene mudamvera Ambuye ndi kuvomereza poyera polola kuti mufe ndi kuukanso naye kudzera mu ubatizo wa madzi ndipo potero kufanana naye Ambuye Yesu. Malo amenewo a chikumbutso ndi gwero la mphamvu ndi chigonjetso polimbana ndi mdaniyo.

KALOZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: UBATIZO WA MADZI

Malemba: *Chifukwa chache mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.* —Mateyu 28:19

Mwachidule: Okhulupirira mwa Yesu Khristu akulamulidwa kuti abatizike ndi madzi. Pamene timvera ichi pomizidwa munthu yense m'madzi ziyimira imfa, kuukitsidwanso ndi moyo wosandulika umene umalandiridwa kudzera mu kuyeretsedwa kwenikweni ndi mwazi wa Yesu.

Tanthauzo la Ubatizo: Kuchokera ku mau a chiGriki otchedwa *baptizo* amene ayimira kuviyika, kuthibwika, kumizidwa munthu yense m'madzi, kudzadzitsa.

I. Lamulo lakumwamba

- A. Marko 16:15-16 Batizani okhulupirira onse.
- B. Machitidwe 2:38 Petro analangiza chomwecho.

II. Yohane anaphunzitsa chomwecho / Khristu anaonetsa chitsanzo chake

- A. Marko 1:4-5 Yohane alalikira ubatizo wa kutembenuka mtima.
- B. Mateyu 3:16-17 Yesu anabatizika ndi Yohane Mbatizi.

III. Mpingo Woyamba umachita chomwecho

- A. Machitidwe 2:41 Pa tsiku la Pentekoste.
- B. Machitidwe 8:12 Otembenuka mtima a ku Samariya.
- C. Machitidwe 8:35-39 The Mdindo wa ku Etiopiya.
- D. Machitidwe 9:17-18 Mtumwi Paulo.
- E. Machitidwe 10:44-48 A m'banja la Kornelio.
- F. Machitidwe 16:14-15 Lidia wa ku Tiyatira.
- G. Machitidwe 16:30-33 Woyang'anira ndende.
- H. Machitidwe 18:8 Akorinto.
- I. Machitidwe 19:1-7 Ophunzira a ku Efeso.

IV. Batizani "M'dzina la "

- A. Mateyu 28:19 Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.
- B. Machitidwe 2:38 M'dzina la Yesu Khristu.
- C. Machitidwe 10:48 M'dzina la Ambuye.

V. Zoyenerera pa Ubatizo

- A. Machitidwe 2:38 Kulapa.
- B. Machitidwe 2:41 Landirani Mau.
- C. Machitidwe 8:37 Kukhulupirira.
(Onaninso: Marko 16:16; Machitidwe 8:12; Machitidwe 18:8)

VI. Zimene Ubatizo umayimira

- A. Aroma 6:3-4 Imfa, kuyikidwa mmunda ndi chiukitso.
- B. Akolose 2:12 Kuyikidwa mmunda ndi kuukitsidwa ndi Khristu.

VII. Kumizidwa munthu yense

- A. Tanthauzo la mau akuti *baptizo*.
- B. Marko 1:5 Kubatizika mu mtsinje.
- C. Yohane 3:22-23 Yohane anabatiza pamene panali madzi ambiri.
- D. Machitidwe 8:38 Filipo ndi mdindo uja analowa m'madzi.

VIII. Cholinga cha Ubatizo

- A. 1 Petro 3:21 Chitsimikizo cha chikumbumtima choona.
- B. Machitidwe 2:41-42 Mudziwike ndi mpingo.

Kuomba mkota:

Ndipo anamuzaa kuti aimitse gareta; ndipo anatsikira onse awiri kumadzi, Filipo ndi mdindoyo; ndipo anambatiza iye. Ndipo pamene anakwera kuturuka m'madzi, Mzimu wa Ambuye anakwatula Filipo; ndipo mdindo sanamuonanso, pakuti anapita njira yache wokondwera.

— Machitidwe 8:38-39

UBATIZO WA MADZI

Tsatanetsane wa mau othandizira pa kusanthula kwa Mau Mulungu

YESU ANAPERKA CHITSANZO

Yohane Mbatizi anamumiza Yesu m' madzi pomubatiza. Pamene Yesu amatuluka m' madzi muja, Kumwamba kunatseguka ndipo Mzimu Woyera anatsika pa Yesu ngati nkunda. Liwu linamveka kuchokera Kumwamba: "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa, mwa lyeyu ndikondwera" (Mateyu 3:15-17). Ena mwa mau omaliza amene Yesu analankhula kwa ophunzira ake anali malangizo akuti apite ku dziko lonse ndipo akaphunzitse anthu a mitundu yonse ndi kuwabatiza okhulupirira (Mateyu 28:19-20).

UBATIZO NDI SAKRAMENTI

Pali miyambo ingapo kapena madongosolo ochitidwa mowonetsera amene amachitika mu Chipangano Chatsopano. Ubatizo ndi chizindikiro chooneka ndi maso ndipo unalamulidwa ndi kuwonetsedwa chitsanzo chake ndi Khristu. Chifukwa cha ichi ndiwo umodzi mwa ma sakramento atatu amene Akhristu amene kutsatira mu nthawi zino.

Ubatizo umakhumadzana kwambiri ndi ntchito ya chipulumutso. "Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa" (Marko 16:16). Mulungu amafuna kuti munthu aliyense amene walapa abatizike. Pa tsiku la Pentekoste, anthu anamufunsa Petro kuti achite chiyani pamene anali atatsutsika ndi machimo awo. Iye anawayankha kuti; "Lapani, batizidwani yense wa inu m' dzina la Yesu Kristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu..." (Machitidwe 2:37-38). Ubatizo suyenera kutengedwa mwamasewera ndi mopepuka koma uyenera kulemekezedwa monga lamulo la kumwamba lochokera kwa Ambuye.

ZITSANZO ZOCHOKERA M'BAIBULO ZA UBATIZO

Mpingo woyamba unaphunzitsa ndi kuchita mwambo wa ubatizo. Pa tsiku la Pentekoste, anthu pafupifupi 3,000 anapulumutsidwa ndi kubatizidwa (Machitidwe 2:41). Filipo analalikira kwa Asamariya ndipo amuna ndi akazi amene anatembenuka mtima anabatizika (Machitidwe 8:12). Naye mtumwi Paulo anabatizika patangopita kanthawi pang'ono kuchokera pamene anatembenuka mtima pa njira yopita ku Damasiko (Machitidwe 9:17-18). Anthu amitundu ina amene

anali mnyumba ya Kornelio anatsatira chitsanzo cha Ambuye Yesu polandira ubatizo (Machitidwe 10:44-48). Akorinto amene analapa machimo anabatizika, monga mmene anachitira ophunzira a ku Efeso. Woyang'anira ndende, amene amayang'anira Paulo ndi Sila, anapereka moyo wake kwa Yesu ndipo anapulumutsidwa nabatizidwa usiku womwewo. (Machitidwe 16:30-33). Papita zaka pafupifupi 2,000, mchitidwe umenewu wa ubatizo ukuchitikabe pakati pa otsatira Yesu Khristu.

KUMIZIDWA KAMODZI BASI

Yesu anawalamulira ophunzira ake kuti akabatize "...m' dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera" (Mateyu 28:19). Kumizidwa kamodzi mu m' dzina la magawo atatu a Mulungu kumatsatira zimene Khristu analamulira pa za mmene tidzichitira pobatiza.



*"Amene akhulupirira
nabatizidwa
adzapulumutsidwa."
Marko 16:16*

UCHITIDWE NDI OKHULUPIRIRA OKHA

Ubatizo si wa ana kapena wa anthu osapulumutidwa koma akufuna kulowa mu mpingo. Malemba amaphunzitsa za "ubatizo wa okhulupirira." Munthu ayenera kulapa machimo ake napulumutsidwa asanabatizike. Iwo amene anabatizika pa Tsiku la Pentekoste anali iwo amene alandira Mau. Ubatizo umayenderana ndi kukhulupirira ndipo sizingachitikire mwina. Pamene Filipo anagawana uthenga wabwino ndi Mdindo wa ku Etiopiya, mdindoyo anafunsa kuti: "chindiletsa ine chiyani ndisabatizidwe?" Filipo anamuyankha kuti, "Ngati mukhulupirira ndi mtima wanu wonse mungathe kubatizidwa" (Machitidwe 8:36-37). Kutembenuka mtima komanso kukhulupirira mu mphamvu yopulumutsa ya Ambuye Yesu ndizo zoyenereza ndi zofunikira pa ubatizo. Ngati munthu sayamba wakhulupirira ndi

(Yapitirira pa tsamba 6)

(Kuchokera pa tsamba 5)

kulapa, kwa iye ubatizo uli wopanda phindu. Ndi kuononga chabe kwa tanthauzo lenileni ndi cholinga cha ubatizo pamene ana aang'ono ndi osakhulupirira abatizidwa ndi chiyembekezo chakuti pakutero munthuyo akhoza kupeza chipulumutso.

UBATIZO SUPULUMUTSA WOCHIMWA

Ubatizo wa madzi suchotsa machimo m'moyo wa munthu. Palibe kuyeretsedwa kwa uzimu kulikonse kumene kumakwaniritsidwa ndi ubatizo. Popeza "...mwazi wa Yesu Mwama wache utisambitsa kutichotsera uchimo wonse" (1 Yohane 1:7). Munthu wosapulumsidwa amene wabatizika amangotuluka m'madzi ali wochimwa monga mmene analowera m'madzimo. Chipulumutso komanso kuyeretsedwa kwa mtima zimachokera ku chisomo chakumwamba cha chipulumutso kudzera mu mwazi wa Khristu. Munthu akhoza kubatizidwa kokwana ka 20 komabe nakhala wochimwa pokhapokha patakhalakubadwanso kwa uzimu. Ngati sipakhala kufa ku uchimo, ubatizo umangokhala mwambo wopanda ntchito umene phindu lake silioneka.

NDI CHIZINDIKIRO CHA IMFA NDI CHIUKITSO

Ubatizo ndi chizindikiro cha imfa, kuyikidwa m'manda ndi kuukitsidwa kwa Ambuye. Ndi mwambo umene umachitika ngati chionetsero cha kusinthika m'moyo wa munthu amene wabadwanso mwatsopano. "Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Kristu Yesu; tinabatizidwa mu imfa yache? Chifukwa chache tinaikidwa m'manda pamodzi ndi lye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, chotero ifenso tikayende m'moyo watsopano" (Aroma 6:3-4). Pamene munthu akulowa m'madzi, zimayimira kufa ku uzimu kwa moyo wake wakale wauchimo. Pamene watuluka mmadzimo, zimayimira kuukitsidwa ku moyo waufulu ku uchimo mwa Khristu Yesu. Sikuti m'madzimo mumachitika kuyeretsedwa kwina kulikonse koma ichi ndi chizindikiro komanso umboni wa kuyeretsedwa ndi mwazi kumene kunachitika kale. Chinthu ichi chimasindikiza zimene zachitika kudzera mu kumvera Mau.

UBATIZO NDI KUMIZIDWA MUNTHU YENSE

Mau a m'baibulo akuti "ubatizo" amachokera ku chinenero cha chiGriki wotchedwa kuti *baptizo*. Mauwa amatanthauza kumiza, kuviika kapena kuthibwika. Tanthauzo lake likudzichitira umboni kuti ubatizo, monga mmene amaphunzitsira Malembo, ndi kumira m'madzi munthu yense. Zipembedzo zambiri zimawaza kapena kuthira madzi pa munthu nkumanena kuti umenewo ndi ubatizo. Izi zikusiyana ndi chiphunzitso komanso dongosolo la Yesu. Kuthira komanso kuwaza kumaperewera pa chizindikiro chokoma cha ubatizo. Kumiza kwenikweni kumayimira kusinthika kwa moyo umene uchokera mu kufa ndi kuukitsidwa ndi Khristu.

Kumiza kwathunthu kumachitika mu nthawi za mu Baibulo.



Kubatiza okhulupirira mu mtsinje wina ku Pakistan

Yohane Mbatizi anabatiza mu mtsinje wa Yordano (Marko 1:5). Ndime imene ili pa Yohane 3:22-23 ikunena kuti Yohane anabatiza pamene panali madzi ambiri. Izi sizingafunikire ngati munthu abatiza powaza kapeza kuthira. Filipo ndi mdindo uja "anatsikira onse awiri m'madzi" (Machitidwe 8:38). Chofunikira kwambiri, Khristu mwini wake anatsiyira

chitsanzo chakuti iye anamizidwa yense wathunthu m'madzi pa nthawi ya ubatizo (Mateyu 3:16-17).

UMBONI OONEKERA WA NTCHITO YOCHITIKA MKATI

Ubatizo ndi umboni ooneka ndi maso wa ntchito imene Mulungu wachita mkati mwa moyo wanu. Umenewu ndi "funso lake la chikumbu mtima chokoma kwa Mulungu" (1 Petro 3:21). Ubatizo sikuti ummapereka chikumbumtima chabwino koma ndi machitidwe a kumvera ndiponso zimene timanena momveka bwino pamaso pa Mulungu. Anthu amene atsatira Ambuye mu ubatizo akulengeza pamaso pa onse kuti iwo tsopano ndi zolengedwa zatsopano mwa Khristu ndipo kuti iwo ndiwo a banja la Mulungu. Ubatizo, pokhala chionetsero cha chikhulupiriro, ndi wodabwitsa, chochitika chowonekera chimene chimaonetsera khalidwe lathu latsopano mwa Khristu – osati ngati kapolo wa dziko lapansi komano ngati mwana wa Mulungu.

-mws



1. Kodi anthu akhoza kukalowa Kumwamba ngati sanabatizike?

“Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu” (Yohane 3:3). Anthu amene adzapite Kumwamba ndi okhawo amene abadwa mwatsopano ndipo apulumutsidwa mwa chisomo cha Mulungu. Sitipulumutsidwa ndi nthito kapena zina zochitika kunja koma pokhulupirira (Aefeso 2:8-9). Chifukwa cha ichi, sitipulumutsidwa chifukwa cha mchitidwe woonekera wa ubatizo. Kumwamba kudzakakhala anthu amene sanabatizike ndi madzi, koma anakhululukidwa machimo awo ndi mwazi wa Yesu.

Chitsanzo chomveka bwino ndi cha chigawenga chimene chinapachikidwa pa mtanda. “Ndipo ananena, Yesu, ndikumbukireni m'mene mulowa Ufumu wanu. Ndipo Iye ananena naye, Indetu, ndinena ndi iwe, Lero lino udzakhala ndine m'Paradaiso” (Luka 23:42-43). Chigawengacho chinatembenuka mtima pa mtanda ndipo chinalibe mwayi wakuti nkubatizika. Yesu anamulandira ndipo ananena kuti adzakhala naye ku Paradaiso. Pali anthu amene ali ndi mwayi wopemphera kuti alandire chipulumutso, koma sangathe kukhala ndi nthawi m'moyo uno kapena thupi lawo ndi lofooka kwambiri mwakuti sangathe kubatizika. Iwowa sadzakanizidwa kulowa Kumwamba.

Komabe ndi kuchita kusamvera pamene wina asankha mwadala kuti asabatizike pomwe zomuyenereza komanso mwayi

ulipo. Umenewu ukhoza kukhala uchimo ndipo munthuyo akhoza kutaya chipulumutso chake.

2. Ndi chifukwa chiyani Petro kangapo konse anawalamulira anthu kuti abatizike m'dzina la Yesu? Kodi izi zikutsutsana ndi chiphunzitso cha Khristu kuti tibatizike m'dzina la Atate, la Mwana ndi la Mzimu Woyera?

Yesu anaphunzitsa momveka bwino pa Mateyu 28:19 kuti abatize “m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.”



Petro anawauza anthu pa tsiku la Pentekoste “batizidwani...m'dzina la Yesu Khristu” (Machitidwe 2:38). Ndipo polankhula kunyumba kwa Kornelio, Petro; “analamulira iwo abatizidwe m'dzina la Yesu Khristu” (Machitidwe 10:48). Iye samachita zotsutsana ndi chiphunzitso cha Yesu koma amasiyanitsa ubatizo wa chikhristu ndi maubatizo ena onse anthawi imeneyo. Chinthu china chimene chilonso chofunika kwambiri ndicho chakuti anthu ambiri anakhulupirira mwa Mulungu koma iwo anakana Yesu monga mwana wake; ndipo chifukwa cha ichi, anakananso kubatizika m'dzina la Yesu amene ali chidzalo chonse cha Umulungu m'thupi (Akolose 2:9). Iwo amene poyamba anamukana Khristu analamulidwa kuti alengeze poyera za chikhulupiriro chawo mwa Yesu monga Mpulumutsi wao ndi kuvomereza kuti ali ophunzira a Khristu.

Malangizo a Petro sakukana za Utatu Woyera koma akutsindika mfundo

yaikulu imene inayiwaliidwa. Ndikoyenera ndipo ndi mogwirizana ndi Malemba kubatiza anthu m'dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.

3. Kodi munthu amene wasiya mpingo wa chiphunzitso chonyenga ndi kudzalowa mu mpingo umene uli wa anthu oona a Mulungu abatizidwense?

Ubatizo umene suli “ubatizo wa okhulupirira” ndiye kuti suchitika molingana ndi Malemba. Ubatizo wa ana kapena kubatizika pamene munthu akadali mmoyo wauchimo umapeputsa cholinga chenicheni komanso umboni wa ubatizowo. Munthu wotere adzayenera kubatizidwanso pamene wapulumutsidwadi ku uchimo ndipo wabadwa mwatsopano.

Chipulumutso ndi chimene chimamulowetsa munthu mu Mpingo wa Mulungu ndiponso mu chiyanjano ndi anthu a Mulungu. Ngakhale ubatizo wa okhulupirira unachitika mu mpingo wolakwika, Mulungu amalemekezabe ubatizowo monga mmene amachitira ndi ntchito ya chipulumutso. Pamene anthu achoka mumpingo wachinyengo ndi kukakhala mu chiyanjano ndi anthu oyera mtima a Mulungu, ndipo iwo amafunitsitsa kuti asiyaneni ndi kulekana ndi chipembedzo chimene anali nacho poyamba paja. Galo limodzi la umboni umenewo ndiwo kubatizikanso. Ngakhale Baibulo silinena zobatizikanso kachiwiri mwatchutchutchu, ndi zomveka ndithu pamene mwini wake akufuna kuti awonetsere poyera ku dziko lonse za ufulu wake kuchokera ku chipembedzo chonyenga. Ndipo iye amachita izi pobatizikanso. Choncho chili kwa munthuyo motsogozedwa ndi Mzimu Woyera ngati akufuna kubatizikanso kapena ayi akachokera ku mpingo wachinyengo.

-mws



KODI MUKUDZIWA?

Mchitidwe wobatika ndi madzi sunali wachilendo pakati pa Ayuda pamene Yohane Mbatizi anayamba kulalikira ubatizo wa kutembenuka mtima. Mu nthawi ya Chipangano Chakale, ubatizo unali mwambo womusandutsa munthu kuti akhale Myuda. Anthu a chikunja amene amasanduka Ayuda kudzera mu mwambo wakuwayeretsa wa ubatizo kuti akhalaegawo limodzi ndi kumasonkhana nawo anthu a mtundu wa Chiyuda.



Mau a pa
Nyengo Yake

Achenjezeni

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.us

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Wobadwa ndi munthu iwe, ndakuika ukhale mlonda wa nyumba ya Israyeli, m'mwemo mvera mau oturuka m'kamwa mwanga, nundichenjezere iwo. —Ezekiele 3:17

Ngati mulidi mtumiki weniweni wa Uthenga Wabwino, Mulungu wakuikani kukhala ngati mlonda wa anthu ake. Ndinu wolondera kuti mukhale maso ndi kuyang'anira utumiki umene wakusungitsani. Utumiki wanu si ntchito koma ndi maitanidwe kuchokera kwa Mulungu komanso kudzipereka kwanu kwa anthu. Mvetserani Mzimu wa Mulungu ndipo mulole Mau a Mulungu kuti akhale pamwamba pa china chilichonse pamene mukuphunzitsa ndi kulalikira.

Pamene mdani akugwira ntchito yake ndipo miyoyo yambiri ili pa chiopsezo, limeneli ndi chenjezo kuchokera kwa Ambuye. Musaope kuliza lipenga kapena kupanga zakuti mdaniyo awonekere. Anthu amakonda kumva zinthu zimene zimawakomera ndi kuwalimbikitsa. Zimenezo ndi zoyenera ndiponso zofunikira koma tisamayiwale machenjezo a Mulungu. Mabanja ambiri ndi mipingo imene sinakhazikike pa choonadi chifukwa azibusa asiya udindo wao woliza lipenga.

Inu ndi kazembe wa Khristu, ndiponso woyima mmalo mwa Muungu. Muyenera kudiyetsa, kuphunzitsa, kududzula ndi kuchenjeza gulu la nkhosalo. Muwakonde anthuwo ndi kulolera kudzipereka chifukwa cha iwo. Mukhale chitsanzo cha chiyero ndi kudzisunga. Pamene mayesero akula ndipo zinthu zathina, kumbukirani kuti ndinu mtumiki wa Ambuye. Iye mwini adzaima nanu ndi kukuthandizani komanso kukulimbikitsani kuti mukhalebe wokhulupirika.



-mws